

**KATIKISIMU WA MBIRI YA BAIBULO  
MBIRI YA CHIPANGANO CHATSOPANO CHA BAIBULO**

**OYAMBA KALASI (Kalasi Yoyamba)  
(Buku la chitatu mwa atatu)**

Lalembedwa ndi **Rev C.Hanko**  
Lakonzedwa ndi **Rev. J.J.Lim**  
Mwaonjezeredwanso mfundo zina ndi **Pastor David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka komanso A. Mkwinda**  
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe komanso Rev. Precious Kanyowa**

February 2011 edition

**Katekisimu wa mbiri ya M'baibulo- Nkhani za m'Baibulo za chipangano Chatsopano  
(Oyamba kumene Kuphunzira- Buku lachitatu la atatu)**  
Lalembedwa ndi **Rev C.Hanko**  
Lakonzedwa ndi **Rev. J.J.Lim**  
Mwaonjezeredwanso mfundo zina ndi **Pastor David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** ndi **A. Mkwinda**  
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** ndi **Rev. Precious Kanyowa**

Buku leni leni loyambilira limene ananthauzira ndi **Rev C. Hanko** eni ake ndi a Protestant  
Reformed Churches of America  
Buku ili lakonzedwanso ndi **Rev. J.J. Lim** mu 2011 mothandizidwa ndi Pilgrim Covenant Church.

Chichewa version © 2012 Gratia Dei Sola Media  
Lasindikizidwa ndi Grata Dei Sola Media  
Blk 203B, Henderson Road , No. 07-07, Singapore 159546  
Website: [www.gdsmedia.org](http://www.gdsmedia.org)  
Email: [gdsmedia.sg@gmail.com](mailto:gdsmedia.sg@gmail.com)

Palibe akuloledwa kusindikiza kapena kuchulukitsa buku ili ngakhale za mkatimu

**Synod ya Evangelical Presbyterian Church (EPC) ku Malawi ndi ku Mozambique  
inavomereza mu chaka cha 2012 kuti bukuli lizigwiritsidwa  
ntchito mu mipingo yawo yonse.**

## **MAWU A MLEMBI**

Ili ndi buku la chitatu la ena la magawo a katikisimu lomwe limakhuza nkhanzi za m'baibulo kwa ana a zaka za pakati pa zisanu ndi chimodzi kufikira zaka zisanu ndi zitatu. Mabuku awiri oyambirira akamba za chipangano chakale koma buku ili likukamba za chipangano cha tsopano.

Phunzilo ilionse likukamba za mbali imodzi ya mbiri osati kulowa kwambiri mozama mu zochitika. Komanso mfundo za mbiriyi azitsindikiza paliponse pofunka moyenera ngati nkotheka maka kothera kwa phunziro. Mphunzitsi yekha ayenera kusankhula mozindikira kuti ndiziti zomwe angaphatikize pa phunziro mkalasi yake.

Magawidwe ofanana otere a ntchitoi akugwiritsidwano ntchito mu "Lolani Ana" yomwe analemba Mrs Getrude Hoeksema, ndicholinga chopanga mgwirizano pakati pa zophunzira kusukulu ndi mukatikisimu nthawi zonse pamene mabuku onse akugwiritsidwa ntchito.

Mafunso ndi mayankho a buku lobwerezari ndiwotalikapo kusiyana ndi loyamba. Tifuna kuti ana ang'ono aphunzire mokwanira ndipo ana okulirapo aphunzire phunziro lonse.

Ndipo zisomo za malonjezano za Ambuye zithandize kugwiritsa ntchito bukuli pophunzitsira moyenera ndikukhazikika mu uzimu kwa ana athu. Kwa Iye ndi chiyembekezo chathu ndipo kwa Iye yekha kukhale ulemelero ku miyoyo yathu.

- Rev. C.Hanko

## **MAWU A MKOZI**

Kagwiritsidwe ntchito ka katikisimu wophunzitsira ana mu mpingo ndi njira ya bwino komanso yothandiza. Mabuku atsopanowa apangidwa pofuna kudzamitsa mizu pa mfundo za M'baibulo ndi mbiri zomwe zingapangitse kuti akhale ndi chiyambi mu ziphunzitso cha katikisimu monga Katekisimu Wachidule wa Westminister.

Malembedwe amakono a Katikisimu a mbiri ya Baibulo(a Feb 2011 edition) adutsa mumisintho yosiyanasiyana pofufuza mfundo ndi zolakwika mkalementedwe mu mabuku oyambirira; komanso kufufuza za kawerengedwe ndi maganizo a mkozi a Pastor David Higgs. Ntchito ya kapangidwe ka mawu ambiri a mafunso ndi mayankho kakhalanso kosinthika (pothandizira zotsatira kuchokera kwa kwa makolo) kuti malowezedwe akhale osavuta kwa ana athu. Mfundo zapadera zaperekedwa mowonjezera kwa makolo ndi aphunzitsi kuti agwiritse ntchito. Izi zakonzedwa ndi Pastor Higgs.

Buku lina logwiritsira ntchito lophatikiza ku buku ili lapangidwa. Makolo akulimbikitsidwa kuthandiza ana kuchita ntchito yokhazikika powonjezera kuthandiza kuloweza mayankho ku mafunso khumi sabata iliyonse. Monga udindo wa aphunzitsi a school yasabata ndikukhala okwaniritsa makolo maka abambo ali olimbikitsidwa kuphunzitsa ana awo moyenera asanapite mkalasi. Akafika mkalasi aphunzitsi amangowauza mochepa chabe maphunziro ongofuna kuganiza basi ndipo amangowunikira phunzirolo ndi mwana aliyense powayesa ntchito zomwe iwo akukumbukira.

Ambuye wathu adalitse maganizo athu ochepa kuti athandizire kulangiza ana athu mu njira ya Mulungu.

- Pastor J.J. Lim

**PHUNZIRO 1**  
**YOHANE MBATIZI**  
**Luka 1**

**1. Kodi mngelo Gabrieli anawonekera kwa yani ?**

Kwa Zakaliya mkachisi . (Lk 1:5; 8-11)

**2. Kodi mngelo anamuwuza chiani Zakaliya?**

Anamuwuza kuti adzakhala ndi mwana wa mwamuna. (Luka 1:13)

**3. Kodi Zakaliya anawuzidwa kuti mwana wake adzamutcha ndani?**

Anamuwuza kuti adzamutcha Yohane. (Luka 1:13)

**4. N'chifukwa chiani Zakaliya sanakhulupirire?**

Chifukwa iye ndi Elizabeti anali okalamba. (Luka 1:7,18)

**5. Kodi Zakaliya analangidwa bwanji posakhulupirira zomwe anawuzidwa ndi mngelo?**

Anakhala osayankhula ndi osamva kufikira Yohane anabadwa. (Luka 1:19-20)

**6. Kodi izi zinalanga bwanji Zakaliya?**

Sanathe kufotokoza za nkhani yonse imene mngelo uja anabweretsa. (Luka 1:22, 63, 67)

**7. Kodi Zakaliya anachita chiani pamene anayamba kuyankhula?**

Analemekeza Mulungu kamba ka mwana wofunika amene Mulungu anampatsa. (Luka 1:64)

**8. Kodi chofunika kwambiri pa Yohane M'batizi ndi chiani?**

Anayitanidwa kuti akonzekeretse kubwera kwa Mpulumutsi. (Luka 1:76)

**9. Kodi Yohane anakonza bwanji njira?**

Anawawuza anthu kuti alape ndikuyang'ana kwa Mpulumutsi olonjezedwayo. (Luka 1:77-79; Mateyu 3:1-3)

**10. Ndi chifukwa chiani Yohane anatchedwa mbatizi?**

Chifukwa anabatiza iwo amene analapa machimo ndi kukhulupirira kubwera kwake kwa mpulumutsi. (Mariko 1:2-4)

**VESI LOLOWEZA:**

" Taonani, ndidzatuma Mthenga Wanga kuti akonzeretu njira ndisanafike ine" (Malaki 3:1)

**PHUNZIRO 2**  
**ALENGEZA ZA KUBADWA KWA YESU**  
**Luka 1**

**1. Kodi Mpulumutsi wanu ndi ndani?**

Ambuye Yesu yemwe dzina lake litanthauza "Yehova amapulumutsa" (Luka 1:31; Onaninso Mateyu 1:21)

**2. N'chifukwa chiani anamutcha kuti Yesu zimene zikutanthauza kuti "Yehova amapulumutsa"?**

Amapulumutsa anthu kumachimo awo. (Mateyu 1:21)

**3. Anatumizidwa ndani kuti akanene za kubadwa kwa Yesu?**

Mngelo Gabriel anatumizidwa kuchokera kumwamba. (Luka 1:26)

**4. Mngelo Gabrieli anatumizidwa kwa yani?**

Kwa Maria yemwe anali wa ku fuko la Davide. (Luka 1:27)

**5. Kodi Mngelo Gabriel anamuza chiani Maria ?**

Kuti adzakhala mayi wa Ambuye Yesu. (Luka 1:31)

**6. Kodi mngelo Gabriel anamuza chiani Maria zokhuza Ambuye Yesu?**

Kuti Iye wobadwayo ndi mwana wa Mulungu? (Luka 1:32)

**7. Ndi chifukwa chiani Maria anapita kwa Elizabeti?**

Gabriel anamuza iye kut Elizabeti adzakhala ndi mwana wa mwamuna. (Luka 1:36-40)

**8. Kodi chinachitika ndi chiani pamene Elizabeti anamva Maria akupereka moni?**

Mwana Yohane analumpha ndikukondwera mmimba mwake. (Luka 1:41,44)

**9. Kodi Maria anakhala ndi Elizabeti nthawi yayitali bwanji?**

Kwa miyezi itatu kufikira Yohane anabadwa. (Luka 1:56)

**10. Kodi Elizabeti anawonetsa chisangalalo chake motani pakubwera kwa Mpulumutsi?**

Analemekeza Mulungu pa zodabwitsa zake zonse. (Luka 1:42-55)

**VESI LOLOWEZA:**

" chifukwa chachenso Choyeracho chikadzabadwa chidzatchedwa Mwana wa Mulungu". (Luka 1:35)

**PHUNZIRO 3**  
**KUBADWA KWA YESU**  
**Luka 2**

**1. Chinachitika ndi chiani Yesu atasala pang'ono kubadwa?**

Kaisara Augusto analengeza kuti anthu onse alembetse kalembera. (Luka 2:1-2)

**2. Ndi chifukwa chiani Mulungu anapangitsa kuti lamuloli lichitike?**

Amafuna kuti Yesu akabadwire ku Betelehemu. (Luka 2:3-6)

**3. Ndi chifukwa chiani Mulungu anafuna kuti Yesu abadwire mu Betelehemu?**

Amafuna kuti awonetse zoti Yesu ndi wa kubanja la fuko la Davide. (Luka 2:11; onaninso Mateyu 1:6, 16-17)

**4. Ndichifukwa chiani Yesu anabadwira modyera ng'ombe?**

Chifukwa choti munalibe malo ogona alendo. (Luka 2:7)

**5. Kodi kubadwa kwa Yesu mukhola la ng'ombe chimasonyeza chiani kwa ife?**

Kuti akhale mphawi cholinga ifeyo tikhale olemera. (Luka 2:7; onaninso Afilipil 2:6-7; 2 Akorinto 8:9)

**6. Kodi Mulungu anatuma kwa yani mngelo kukalengeza za kubadwa kwa Yesu?**

Kwa abusa oweta ng'ombe usiku. (Luka 2:8-10)

**7. Kodi mngelo anaiza chiani abusa a ng'ombe?**

"Pakuti wakubadwirani lero mu mzinda wa Davide mpulumutsi amene ali Khristu Ambuye" (Luka 2:11)

**8. Kodi angelo kumwamba amayimba kuti chiani?**

Ulemerero ukhale kwa Mulungu kumwambamwamba ndi mtendere pansi pano, kwa anthu amene akondwera nawo. (Luka 2:14)

**9. Ena amene anadziwanso za kubadwa kwa Yesu ndi ndani?**

Anzeru akummawa omwe anaona nyenyezi kummawa. (Mateyu 2:1-2)

**10. Kodi anzeru a kummawa anachita chiani atawona Yesu?**

Anamulambira Iye ndipo anampatsa mphatso. (Mateyu 2:9-11)

**VESI LOLOWEZA :**

"Kuti chifukwa cha inu anakhala osauka, angakhale anali wolemera, kuti inu ndi kusauka kwake mukakhale olemera." (2 Akorinto 8:9)

**PHUNZIRO 4**  
**MOYO WA YESU M'MASIKU OYAMBIRIRA**  
**Mateyu 2; Luka 2**

**1. Kodi Makolo a Yesu anamutengera kuti atatha masiku makumi anayi?**

Makolo ake anamutengera Iye ku kachisi (Luka 2:21-24, 27; onaninso Lev 12:1-4, 6)

**2. Kodi Yesu anakumana ndi yani mu kachisi?**

Anakumana ndi Simiyoni yemwe anauzidwa kuti sadzafa kufikira atamuona Yesu. (Luka 2:25-27)

**3. Kodi Simiyoni ananena chiani atamulandira Yesu m'manja mwache?**

'Ambuye. tsopano lolani ine ,kapolo wanu ndichoke mumtendere. pakuti maso anga awona mpulumutsi'. (Luke 2:29, 30)

**4. Winanso anabwera ku kachisi pa nthawi imeneyi anali yani?**

Anna mneneri wamkazi yemwe anali okalamba wa zaka makumi asanu ndi mphambu Zitatu (84). (Luka 2:36-37)

**5. Kodi Anna anachita chiani ataona Yesu?**

Anayamika Mulungu poti mpulumutsi wafika. (Luka 2:38)

**6. Kodi mfumu Herodi anamva bwanji za kubadwa kwa Yesu?**

Anzeru akum'mawa anafika kufuna kuona mfumu ya Ayuda. (Mateyu 2:1-3)

**7. Kodi Herodi anachita zotani atawona kuti anzeru a kum'mawa sakubwerera kwa iye?**

Anapha ana onse amuna osapitirira zaka ziwiri mu Betelehemu. (Mateyu 2:16-18)

**8. Kodi Mulungu anateteza bwanji Yesu?**

Anauza Yosefe kuti athawe ndi mwana Yesu kupita ku Aiguputo? (Mateyu 2:13-15)

**9. Kodi Yesu anachita chiani mukachisi ali ndi zaka khumi ndi ziwiri?**

Anali pakati pa aphunzitsi kumva ndi kufunsa mafunso ovuta. (Luka 2:42-47)

**10. Kodi Yesu ananena chiani kwa Maria pamene anampeza Iye m'kachisi?**

"Simukudziwa kuti Ine ndiyenera kupeze ka mnyumba ya Atate Wanga?" (Luka 2:49)

**VESI LOLOWEZA:**

"Ndinaitana Mwana wanga aturuke m'Aiguputo"(Mateyu 2:15b)

**PHUNZIRO 5**  
**YOHANE ABATIZA YESU**  
**Luka 3; Mateyu 3,4**

**1. Kodi Yohane Mbatizi amalalikira kuti?**

Analalikira mchipululu kufupi ndi mtsinje wa Yorodani. (Mateyu 3:1; Luka 3:2-3)

**2. Kodi Yohane amavala bwanji?**

Amavala chovala cha ubweya wangamira ndi lamba m'chiuno mwache. (Mateyu 3:4)

**3. Kodi Yohane amadya chiani?**

Amadya zombe ndi uchi. (Mateyu 3:4)

**4. Nchifukwa chiani anthu anabwera kudzamvera Yohane?**

Anamva kuti mneneri wamkulu wafika pakati pavo. (Mateyu 3:3, 5)

**5. Kodi Yohane amalalikira zotani?**

Anawauza anthu kuti mpulumutsi wafika. (Luka 3:4-6, 16-17)

**6. Anawauza anthu kuti adzitani?**

Anawauza anthu kuti alape machimo awo ndikuyang'ana kwa Mpulumutsi? (Mateyu 3:2, 8, 11-12)

**7. Ndani anabwera kwa Yohane pamene iye anali kulalikira?**

Yesu anabwera kwa Yohane kuti abatizidwe. (Mateyu 3:13)

**8. Chinachitika ndi chiani pamene Yesu anabatizidwa?**

Mzimu woyera anafika pa iye ngati nkhunda. (Mateyu 3:16-17; Luka 3:21-22)

**9. Kodi mzimu woyera unatengera kuti Yesu?**

Kuchipululu komwe anayetsedwa ndi satana. (Mateyu 4:1)

**10. Kodi Yesu anachita chiani atayetsedwa kachitatu?**

Anamuthamangitsa satana ,nanena kuti "Choka satana" (Mateyu 4:10)

**VESI LOLOWEZA:**

"Choka satana pakuti kwalembedwa,Ambuye Mulungu wako udzamgwadira, ndipo Iye yekha yekha adzamulambira. (Mateyu 4:10)

**PHUNZIRO 6**  
**YESU AYAMBA UTUMIKI WAKE**  
**Yohane 2-3**

**1. Kodi Yesu anapita kuti ndi ophunzira ake asanu ndi mmodzi?**

Anapita ku ukwati ku Kana wa Galileya. (Yohane 2: 1-2)

**2. Kodi Maria amayi a Yesu anaiza chiani Yesu nthawi ya mgonero?**

Anamuza Iye kuti vinyo watha. (Yohane 2:3)

**3. Kodi Yesu anaiza antchito kuti apange chiani?**

Anawauza kuti adzadze mbiya zisanu ndi imodzi ndi madzi. (Yohane 2:6-8)

**4. Kodi Yesu anapanga chiani antchito atatha kudzadza mbiya ndi madzi?**

Anasandutsa madzi kukhala vinyo. (Yohane 2:9-10)

**5. Kodi chotsatira cha chodzizwa choyamba chimenechi chinali chotani?**

Ophunzira a Yesu anadziwa kuti Iye ndi mpulumutsi olonjezedwa. (Yohane 2:11)

**6. Kodi Yesu anapita kuti atachoka pa ukwati wa ku Kana?**

Anapita ku Yerusalemu kuti akakhale nao pa mgonero wa pasaka. (Yohane 2:13)

**7. Kodi Yesu anapanga chiani mu kachisi?**

Anakwapula ndikuthamangitsa ogula ndi ogulitsa malonda (Yohane 2:14-16)

**8. Kodi ichi chinapangitsa atsogoleri Achiyuda kukwiya?**

Inde, ndipo zinapangitsa kuti amufunse kuti Iye wapanga zotere ndi udindo wanji? (Yohane 2:18)

**9. Kodi Yesu anawayankha chiani?**

"Ndidzawononga kachisi ndikumanga masiku atatu. (Yohane 2:19)

**10. Ndi phunziro lanji lofunika limene Yesu anaphunzitsa Nekodemo?**

"Ngati munthu sabadwa mwa tsopano, sakhoza kuona ufumu wa Mulungu" (Yohane 3:3)

**VESI LOLOWEZA:**

"Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi,kotero anapatsa mwana wobadwa yekha,kuti yense okhulupirira Iye asatayike koma akhale nawo moyo wosatha. (Yohane 3:16)

**PHUNZIRO 7**  
**YESU PACHISIME KU SAMARIYA**  
**Yohane 4**

**1. Kodi Yesu anapita kuti kuchokera ku Yerusalemu anatha pasaka?**

Anachoka ku Samariya ndikupita ku Galileya. (Yohane 4:1-4)

**2. Kodi Yesu anakumana ndi yani pa chisime ku Samariya?**

Anakumana ndi msamariya wachikazi yemwe anabwera kudzatunga madzi. (Yohane 4:4-7)

**3. Kodi Yesu anafunsa chiani msamariya wachikazi uja?**

Anamufunsa, "Undipatse madzi ndimwe" (Yohane 4:7a)

**4. Kodi Yesu anamuza chiani msamariya wachikazi?**

Anamuza kuti Iye ndi madzi amoyo. (Yohane 4:10, 14)

**5. Kodi Yesu amatanthauza chiani ponena kuti Iye ndi madzi a moyo?**

Amatanthauza kuti Iye ndi mpulumutsi yemwe anabwera kuti apulumutse tonse ku machimo ndi imfa. (Yohane 4:13, 14; onaninso Yohane 3:36; 7:37)

**6. Kodi Yesu anachita chiani pamene anali kuyakhula ndi mzimayi wa Samalia?**

Anamuchititsa iye kuti akhulupirire Iye ngati mpulumutsi wake. (Yohane 4:25-26, 29)

**7. Kodi mzimayi wa ku Samaliya anachita chiani pamene anakhulupirira zoti Yesu ndi mpulumutsi wake.?**

Anapita mu mzinda ndikuwuza anthu kuti onse abwere ndikumva kwa Yesu. (Yohane 4:28-30)

**8. Kodi Yesu anapulumutsanso anthu ku Samaria?**

Inde, ambiri anakhulupirira kuti Iye ndi mpulumutsi wao. (Yohane 4:39-42)

**9. Kodi izi zinasyeza chiani kwa ophunzira ache?**

Zinasyeza kuti Mulungu adzasonkhanitsa anthu ake ngakhalenso amitundu. (Yohane 4:9, 27, 35-38; Mateyu 28:19-20)

**10. Kodi Yesu anakhala nthawi yayitali bwanji ku Samaria?**

Anakhala masiku awiri ndipo anapita ku Galileya. (Yohane 4:43)

**VESI LOLOWEZA:**

"Moyo wanga uli ndi ludzu la kwa Mulungu wa moyo. (Masalimo 42:2a)

**PHUNZIRO 8**  
**YESU APHUNZITSA KU GALILEYA**  
**Yohane 4, Luka 4**

**1. Kodi Ayudaanasangalala kuona Yesu ku Galileya?**

Inde, chifukwa anafuna kuona zozizwa zambiri. (Luka 4:14; Yohane 4:45; 2:23)

**2. Kodi ndichodabwitsa chiti chachiwiri chomwe Yesu anachitaa ku Kana?**

Anachiza mwana wa mkulu wina wa mfumu (Yohane 4:46, 50, 54)

**3. Kodi mkulu wa mfumu wa Kana amakhala kuti?**

Amakhala ku Kaperenao ulendo wa mtunda (ma mailosi) makumi awiri. (Yohane 4:46)

**4. Kodi Yesu anachiza bwanji mwana wa mkulu wa mfumu?**

Anamuza mawu ndipo mwanayo anachila. (Yohane 4:50,53)

**5. Kodi Yesu anapita kuti atachoka ku Kana?**

Anapita ku Nazareti komwe Iye anakulira. (Luka 4:16)

**6. Kodi Yesu anaphunitsa chiani ku Nazareti?**

Anawauza kuti Iye ndi kristu wolonjezedwayo yemwe mneneri Yesaya analosera. (Luka 4:17-19; onaninso Yesaya 61:1)

**7. Kodi anthu aku Nazareti anamukhulupirira Yesu?**

Ayi, sanakhulupirire kuti Iye ndi khristu wolonjezedwa. (Luka 4:20-22, 28-29)

**8. Kodi Yesu anawauza chiani anthu aku Nazareti pamene iwo sanakhulupirire Iye?**

Anawauza kuti uthenga ufikira anthu amitundu. (Luka 4:24-27)

**9. Kodi anthu anapanga chiani pamene anamva zimenezi?**

Anakwiya kwambiri ndipo anafuna kumukankhira ku phompho. (Luka 4:28-29)

**10. Kodi Yesu anapulumuka bwanji ku chiwembu chimenechi?**

Iye anadutsa pakati pao ndipo anachokapo osamukhudza. (Luka 4:30)

**VESI LOLOWEZA:**

"Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, chifukwa chache Iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka uthenga wabwino"(Luka 4:18)

**PHUNZIRO 9**  
**YESU ACHIRITSA PA SABATA**  
**Yohane 5**

**1.Ndi chifukwa chiani Yesu anapita ku Yerusalemu kachiwiri?**

Anapita kuti akakhale nao pa phwando la Ayuda. (Yohane 5:1)

**2.Kodi Yesu anapita kuti tsiku la sabata pamene anali ku Yerusalemu?**

Iye anapita ku thamanda la Betisaida komwe kunali odwala ambiri. (Yohane 5:2, 8-9)

**3.Ndi chifukwa chiani anthu amapezeka pa thamanda limeneli?**

Amakhulupirira kuti mngelo amabwera ndikuvundula madziwo ndipo munthu oyamba kugweramo amachiritsidwa. (Yohane 5:4)

**4.Kodi Yesu anayankhula kwa yani?**

Kwa munthu yemwe anali olumala kwa zaka makumi atatu kuza zisanu ndi zitatu (38) (Yohane 5:5)

**5.Kodi munthu opuwala amaonetsa chithunzithuzi chanji?**

Amaonetsa chithunzithuzi kwa ife monga anthu ochimwa. (Yohane 5:14, 19-25; onaninso Aefeso 2:1-5; Yesaya 35:5-8; 61:1-3)

**6.Kodi Yesu ananena chiani kwa munthu opuwala uja?**

"Tauka yalula mphasa yako nuyende". (Yohane 5:8)

**7.Kodi Afarisi anakondwa kuona munthu opuwala atachiritsidwa?**

Ayi, anali okwiya kamba koti ananyamula mphasa yake pa tsiku la sabata. (Yohane 5:9-10)

**8.Kodi Afarisi ananena chiani pamene anamva kuti Yesu anachiza munthu opuwala uja?**

Ananena kuti Yesu waswa sabata. ( Yohane 5:15-16)

**9.Kodi Yesu anaswa sabata pochiza munthu wopuwala uja?**

Ayi, Yesu ndi Ambuye wa sabata, ndipo kugwira ntchito yabwino pa sabata sitchimo. (Yohane 5:17; Mateyu 12:7-8)

**10.Kodi zitanthauza chiani zoti Yesu ndi Ambuye wa sabata?**

Zitanthauza kuti sabata ndi tsiku la Ambuye, tsiku limene mwini wake ndi Iyeyo. (Mariko 2:27-28; Chivumbulutso 1:10)

**VESI LOLOWEZA:**

"Motere Mwana wa munthu ali mwini dzuwa la Sabata lomwe". (Mariko 2:28)

**PHUNZIRO 10**  
**YESU PA NYANJA YA GALILEYA**  
**Luka 8 ndi Mateyu 8**

**1. Kodi chinachika ndi chiani pamene Yesu ndi ophunzira anaolokera ku tsidya la nyanja ya Galileya?**

Mphepo yankuntho inabuka pa nyanja. (Luka 8:23)

**2. Kodi ophunzira ake anaopa?**

Inde, amaopa kuti bwato lao lingamire. (Luka 8:24)

**3. Kodi Yesu amachita chiani nthawi ya namondweyi?**

Anali ntulo tambiri mubwatolo. (Luka 8:23a; Mateyu 8:24)

**4. Kodi Yesu anapanga chiani pamene anamudzutsa?**

Analamulira mphepo kuti ikhale bata ndipo nyanja inamvera Iye. (Luka 8:24b; Mateyu 8:26)

**5. Kodi Yesu anawaphunzitsa chiani ophunzira ake za mphepo imeneyo?**

Anawaphunzitsa iwo zoti ali otetezedwa nthawi zonse ndi Iye. (Luka 8:25; onaninso Yesaya 43:2)

**6. Kodi Yesu anakumana ndi yani ku tsidya lina la nyanja?**

Anthu awiri ogwidwa ndi ziwanda. (Mateyu 8:28)

**7. Kodi Yesu analamulira kuti ziwandazi zitani?**

Analamulira kuti zichoke mwa iwo. (Mateyu 8:32)

**8. Kodi chinachitika ndi chiani pamene Yesu analamulira ziwanda kuti zilowe mwa nkhumba m'mbali mwa phiri?**

Nkhumba zinathamangira ku nyanja ndipo zonse zinamira. (Luka 8:33)

**9. Kodi Yesu anatiphunzitsa chiani pa mphamu yachevi pa satana?**

Amatiphunzitsa kuti ngakhale a satana palibe chirmene angachite kupatula mphamu imene Mulungu amapereka kwa iwo. (Mateyu 8:29-31; Luka 4:41; 2 Petulo 2:4)

**10. Kodi anthu a ku Geresa anakhulupirira Yesu pamene anaona zodabwitsa za mphamu yache?**

Ayi, iwo anafuna nkhumba zao osati Yesu. (Luka 8:37)

**VESI LOLOWEZA:**

"Ndiye munthu wotani uyu, pakuti ngakhale mphepo ndi nyanja zimvera Iye" (Mateyu 8:27b)

**PHUNZIRO 11**  
**ANTHU AFUNA YESU KUKHALA MFUMU YAO**  
**Yohane 6**

**1. Kodi ndichozizwa chanji chimene Yesu anapanga m'chipululu kufupi ndi Kaperenao?**  
Anadyetsa makamu a wantru zikwi zisanu (5000) kupatula akazi ndi ana. (Yohane 6:10)

**2. Ndi chifukwa chiani chimenechi chinali chozizwa chachikulu?**

Chifukwa Yesu anawadyetsa anthuwa ndi mikate isanu ndi tinsomba tiwiri ndipo anatolera makombo mandengu khumi ndi awiri. (Yohane 6:9, 11-13)

**3. Kodi Yesu anawaphunzitsa chiani anthu kupyolera mu chozizwa chodyetsa zikwi zisanu?**

Anawaphunzitsa kuti Iye ndi mkate weniweni wochokera kiumwamba. (Yohane 6:32-35)

**4. Chinachitika ndi chiani kwa ophunzira a Yesu pamene anafuna kuolokera ku tsidya la nyanja?**

Mulungu anatumiza chimphepo pa nyanja kuti asakafike ku tsidya lina. (Yohane 6:16-18)

**5. Kodi Yesu anawathandiza bwanji?**

Anabwera akuyenda pa nyanja ndipo analetsa chimphepocho. (Yohane 6:19)

**6. Kodi Yesu anawaphunzitsa chiani ophuzira poyenda kupita kwa iwo pa mafunde?**

Ngakhale mpingo ungadutse mu mphepo zambiri, Yesu nthawi zonse adzakhala pafupi nafe. (Yohane 6:20-21; Aefeso 1:19-23)

**7. Ndi chifukwa chiani anthu ena anali kumufuna Yesu mbali ina ya nyanja?**

Amafuna kuti Yesu akhale mfumu yao ya dziko chifukwa anawadyetsa modabwitsa. (Yohane 6:15)

**8. Kodi Yesu amafuna kuti akhale mfumu ya dziko?**

Ayi, anawauza anthu aja kuti ufumu wake ndiwakumwamba. (Yohane 6:36-41)

**9. Kodi anthu anasonyeza bwanji kuti samafuna ufumu umenewo?**

Ambiri anabwerera m'mbuyo ndipo sanayenda-yendanso ndi Iye. (Yohane 6:66)

**10. Kodi ophunzira anayankha chiani pamene Yesu anawafunsa kuti ngati anafuna kuchoka kwa Iye?**

Anayankha Iye, "Ambuye ,tidzamuka kwa yani? Inu muli nao mau a moyo wosatha. (Yohane 6:68)

**VESI LOLOWEZA:**

"Ine ndine mkate wamoyo wotsika kumwamba". (Yohane 6:51a)

**PHUNZIRO 12**  
**MAWALITSIDWE A YESU PAPHIRI**  
**Mateyu 16,17**

**1.Kodi Yesu anawauza chiani ophunzira ake atalapa kuti Iye ali mawu a moyo osatha?**  
Anawauza iwo kuti Iye ayenera kuzunzika ndi kufa . (Mateyu 16:21)

**2.Kodi Iye anawauzanso chiani?**  
Anawauzanso kuti Iye adzauka kwa akufa. (Mateyu 16:21)

**3.Kodi Yesu anatenga ndani pa phiri lalitali pa okha?**  
Ophunzira ake atatu: Petulo, Yakobo ndi Yohane. (Mateyu 17:1)

**4.Chinachitika ndi chiani pamene Yesu amapemphera pa phiri?**  
Nkhope yake inawala ngati duwa ndipo zovala zake zinayera ngati matala. (Mateyu 17:2)

**5.Ndi ndani anaonekera kwa Yesu pamenepo?**  
Mose ndi Eliya omwe anayankhula kwa Iye zokhuza imfa yache. (Luka 9:30-31)

**6.Kodi mawu ochokera kumwamba ananena chiani?**  
Ananena kuti "Uyu ndimwana wanga okondedwa mwa Iyeyu ine ndikondwera". (Mateyu 17:5)

**7.Ndi chozizwa chanji chimene Yesu anachita m'mawa atasandulika?**  
Anachiza mnyamata wodwala khunyu (Mateyu 17:15, 18)

**8.Kodi abambo a mnyamata ananena chiani kwa Yesu?**  
Anati "ndikhulupirira ; thandizeni kusakhulupirira kwanga". (Mariko 9:24)

**9.Kodi chosaiwalika pa chozizwa chimenechi ndi chiani?**  
Ophunzira anayesera koma sanathe kuchiza mnyamata. (Mateyu 17:16, 19)

**10.Kodi chozizwa chimenechi chikutiphunzitsa chiani?**  
Kuti tiyenera kukhulupirira kuti palibe choipa chachikulu choti Yesu sangachithetse.  
(Mateyu 17:18; Masalimo 130:7-8; Aheberi 7:25; 1Timoteo 1:15)

**VESI LOLOWEZA:**

"Ndipo onse anadabwa pa ukulu wache wa Mulungu"( Luka 9:43)

**PHUNZIRO 13**  
**YESU APHUNZITSA MU YERUSALEMU**  
**Yohane 8-9, 12 ndi Luka 10:38-41**

**1. Kodi Yesu amakhala kuti pamene amakonzekera phwando la pasaka  
ku Yerusalem?**

Amakhala kunyumba ya Maria, Marita ndi Lazaro ku Betaniya. (Yohane 12:1-3)

**2. Kodi Malita anaonetsa chikondi bwanji kwa Ambuye?**

Iye anatekeseka ndi kutumikira popereka chakudya. (Luka 10:40; Yohane 12:2)

**3. Kodi Maria anawonetsa chikondi chake motani kwa Ambuye?**

Anamvetsera Iye pamene anali kuphunzitsa za ufumu wa kumwamba. (Luka 10:39)

**4. Kodi Yesu ananena chiani za Maria?**

Ananena kuti Maria anasankha chithu chabwino chomwe sichidzachokeka kwa iye. (Yohane 10:42)

**5. Kodi Yesu anaphunzitsa chiyani mu kachisi?**

Anawaphunzitsa zoti Iye ndi Mpulumutsi, Kuunika kwa Dziko. (Yohane 8:2, 12)

**6. Kodi izi zinakwiyitsa bwanji olamula?**

Anaganiza kuti Yesu amangonama chabe za Iye ndipo amanyoza dzina la Mulungu. (Yohane 8:13, 58-59)

**7. Kodi Yesu anapulumuka bwanji pamene anafuna kumugenda mwala?**

Anabisala Iye pakati pao natuluka m'kachisi. (Yohane 8:59)

**8. Ndi chozizwa chanji chimene Yesu anapanga atafuna kuponya miyala m'kachisi muja?**

Anachiza wakhungu yemwe amakhala pa chipata cha kachisi. (Yohane 9:1, 6-7, 11)

**9. Kodi achilamulo ananena chiani za munthu yemwe Yesu anamuchiza ku khungu?**

Ananena kuti munthu ameneyu sanali wa khungu. (Yohane 9:9, 18)

**10. Kodi Yesu anamuchitira chiani munthu wosaona uja?**

Anampatsa maso auzimu omwe anamuthandizira kuona kuti Yesu ndi kuwala kwa dziko lapansi. (Yohane 9:2-4, 27-28, 35-39)

**VESI LOLOWEZA:**

Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi; iye wonditsa ine sadzayenda mumdimba , koma adzakhala nako kuunika kwa moyo. (Yohane 8:12)

**PHUNZIRO 14**  
**YESU AUKITSA LAZARO KWA AKUFA**  
**Yohane 11**

**1. Kodi Yesu anapita kuti pamene Ayuda anafuna kumupha?**

Anapita ku Pereya ku tsidya la Yordano. (Yohane 10:39-40)

**2. Kodi Yesu anaphunzitsa bwanji anthu a ku Pereya?**

Anaphunzitsa anthu ndi mafanizo. (Monga, Luka 15:3, 8, 11)

**3. Tchulani mafanizo atatu omwe Yesu anaphunzitsa ku Pereya?**

" Fanizo la nkosa yotayika, fanizo la ndalamu yotayika, fanizo la mwana wolowerera" (Luka 15)

**4. Ndani anabwera kwa Yesu ku Pereya?**

Amesenjala omwe anamuuya kuti bwenzi lake Lazaro anadwalika. (Yohane 10:40; 11:1-3)

**5. Ndi chifukwa chiani ophunzira anachita mantha kumuperekeza Yesu ku Yerusalem?**

Anachita mantha chifukwa Ayuda anafuna kumupha Yesu (Yohane 11:8; onaninso Phunziro 13, funso 7)

**6. Kodi Tomasi ananena chiani?**

Tiyeni ifenso tipite kuti tikafe naye limodzi. (Yohane 11:16)

**7. Chifukwa chiani Yesu anayembekezera mpaka Lazaro kumwalira?**

Anafuna kuonetsa kuti ali ndi mphamvu zoukitsa akufa. (Yohane 11:14-15, 39-44)

**8. Kodi Yesu anachita chiani pamanda a Lazaro?**

Anamuukitsa Lazaro kwa akufa pofuula ndi mawu akulu. (Yohane 11:43)

**9. Kodi Yesu anaphunzitsa chiani pa zozizwa zazikuluzi?**

Anaphunzitsa kuti Iye ali ndi mphamvu youkitsa anthu ake ku ufumu wa kumwamba. (Yohane 11:25-26)

**10. Kodi zotsatira za chozizwa kwa olamulira zinali zotani?**

Anasinthika maganizo ndikusiya kufuna kupha Iye. (Yohane 11:53)

**VESI LOLOWEZA:**

" Ine ndine kuuka ndi moyo, wokhulupirira Ine angakhale amwalira adzakhala ndi moyo. (Yohane 11: 25)

**PHUNZIRO 15**  
**YESU APITA KU CHIKONDWELERO CHA PASAKA**  
**Luka 18-19 ndi Yohane 12**

**1. Kodi Yesu anapita kuti ataukitsa Lazaro?**

Anapita ku Mzinda wa Efraimu kufupi ndi Yerusalem? (Yohane 11:54)

**2. Kodi Yesu anazera kuti popita ku Yerusalem?**

Anazera ku Yeriko komwe anthu ambiri aulendo amazera popita ku phwando la pasaka. (Luka 18:31, 35)

**3. Kodi Yesu anakuma ndi yani atangotuluka kunja kwa Yeriko?**

Anakumana ndi wosaona Batumeyo yemwe analira," Yesu mwana wa Davide mundichire chifundo. (Luka 18:38)

**4. Kodi Batumeyo anachita chiani pamene Yesu anamuchiza ndikuyambanso kuona?**

Anamuukitsa Iye ndikulemekeza Mulungu. (Luka 18:43)

**5. Ndani anakwera mu mtengo wa mkuyu kuti aone Yesu?**

Zakeyu, wamisonkho yemwe anali wolemera. (Luka 19:2-4)

**6. Kodi Yesu ananena chiani atafika pa Zakeyu?**

"Zakeyu fulumiza tsika mu mtengo , chifukwa lero ndidzakhala kunyumba kwako". (Luka 19:5).

**7. Kodi anthu aku Yeriko anaganiza zotani pamene anamuona Yesu akulowa mnyumba ya Zakeyu?**

Anakwiya kwambiri chifukwa anamuda Zakeyu yemwe anali okhometsa misonkho. (Luka 19:7)

**8. Kodi Yesu anawayankha chiani anthu omwe anakwiya kamba koti anapita kunyumba kwa Zakeyu?**

Anawauza kuti Iye amabweretsa chipulumutso kwa mwana weniweni wa Abrahamu. (Luka 19:9-10)

**9. Kodi Maria wa ku Betaniya anawonetsa chikhulupiriro chake motani kwa Yesu?**

Anadzoza thupi la Yesu ndi mafuta onunkhira. (Yohane 12:3)

**10. Ndi chifukwa chiani Maria anadzoza thupi la Yesu?**

Anakhulupirira kuti Yesu adzafa ndipo adzaukanso kwa akufa. (Yohane 12:7)

**VESI LOLOWEZA:**

"Pakuti mwana wa munthu anadza kufunafuna ndi ndikupulutsa chotayikacho". (Luka 19:10)

**PHUNZIRO 16**  
**YESU ALOWA MUYERUSALEMU MONGA MFUMU**  
**Mateyu 21 ndi Luka 19**

**1. Kodi Yesu anachita chiani pa tsiku loyamba la sabata yomwe anafa?**

Analowa m'Yerusalemu atakwera pa mwana wa bulu. (Mateyu 21:7-12)

**2. Kodi anthu anachita chiani atamuona Yesu atakwera pa mwana wa bulu akulowa m'Yerusalemu?**

Anabwera nayala zovala zao pa njira nadula nthambi za mitengo ya nkunguza. (Mateyu 21:8; Luka 19:36; Yohane 12:13)

**3. Kodi anthu anafuula kuti chiani paneme Yesu amadutsa?**

Anafuula , "Hosana kwa mwana wa Davide". (Mateyu 21:15)

**4. Ndi chifukwa chiani anthu anafuula "Hosana" pamene mawuwa amagwiritsa ntchito kwa mafumu okha?**

Aneneri analogera kuti mfumu idzabwera kwa inu itakwera pa bulu. (onani Zakaliya 9:9; Yesaya 62:11)

**5. Kodi anthu amaganiza kuti Yesu akupanga chiani pamene amalowa m'Yerusalemu ali pa bulu?**

Amaganiza kuti Yesu adzipanga Iye mwini mfumu ya dziko lapansi. (Mateyu 21:5, 8-9)

**6. Kodi Yesu amawasonyeza chiani anthu?**

Amawasonyeza kuti Iye ndi mfumu ya kumwamba. (Mateyu 21:4-5; Luka 19:37-38)

**7. Ndi chifukwa chiani Yesu amawasonyeza izi pa nthawi imeneyi?**

Anatsala pang'ono kulowa muufumu wake. (Mateyu 20:22-23; Luka 22:29-30)

**8. Ndi chifukwa chiani Yesu anakwera pa mwana wa bulu osati bulu wa mkulu?**

Anasonyeza kuti Iye ndiwodzichepetsa ndiwozunzidwa kulowa mu ufumu wa kumwamba. (Onani 2 Akorinto 8:9; Yohane 17: 4-5; Machitidwe 5:30-31)

**9. Chifukwa chiani Yesu anayenera kuvutika?**

Anayenera kuvutika kuti atipulumutse ku machimo athu ndikutitengera kumwamba. (Yesaya 53)

**10. Kodi Yesu adzaonekera pamaso pa anthu onse ngati mfumu yathu?**

Inde, Yesu tsopano ndi mfumu ya kumwamba ndipo adzaoneka ngati mfumu yathu akadzabweranso kachiwiri. (1 Akorinto 15:23-27; Chivumbulutso 1:5-6; 2 Atesalonika 1:7-10)

**VESI LOLOWEZA:**

"Hosana kwa mwana wa Davide! Wolemekezekwa ndiye wakudza m'dzina la Ambuye" (Mateyu 21:9b)

**PHUNZIRO 17**  
**MGONERO WOTSIRIZA**  
**Mateyu 26 ndi Yohane 13**

**1. Kodi Yesu anakonzera kuti chikondwerero cha pasaka wotsiriza?**

Anakonzera chikondwerero cha pasaka pa chipinda cha pa mwamba. (Mariko 14:14-15; Luka 22:11-12)

**2. Kodi choyambirira chimene Ambuye Yesu anachita pa pasaka wa mgonero ndi chiani?**

Anasambisa mapazi a ophunzira ake ngati kapolo. (Yohane 13:3-5)

**3. Ndi chifukwa chiani Yesu anasambisa mapazi a ophunzira?**

Anaonetsa kuti anayenera kuperekayo moyo wake kuti utsuke machimo awo. (Onani Yohane 13:7-8, 10)

**4. Ndi chifukwa chinanso chanji chimene Yesu ananena chimene anasamkitsira mapazi awo?**

Anawauzanso kuti aphunzire kutumikirana wina ndi mnzake. (Yohane 13:12-17)

**5. Kodi chofunika chachiwiri chinachika pa pasaka wa mgonero ndi chiani?**

Yesu anamuuzza Yudasi Esikalioti, "Chimene uchita ,chita msanga". (Yohane 13:27)

**6. Kodi Yudasi anadziwa chimene Yesu amatanthauza?**

Inde, Yudasi anapitilira ndi kukampereka Yesu. (Yohane 13:30; Mateyu 26:25, 47)

**7. Kodi ndichofunika chiti chachitatu chimene Yesu anachita pa pasaka wa mgonero?**

Anaperekayo mkate ndi vinyo kwa ophunzira ngati chizindikiro cha thupi lake ndi mwazi wokhet sedwa. (Mateyu 26:26-28)

**8. Ndi chifukwa chiani ichi chinali chofunika kwambiri?**

Yesu anaperekayo chizindikilo ichi kwa ife kuti chikhale chikumbutso cha mgonero wa Ambuye. (1 Akorinto 11:24-26)

**9. Kodi Yesu anapita kuti utatha mgonero?**

Anapita m'munda wa Getsemani kukapemphera. (Mateyu 26:36)

**10. Kodi anabwera m'Getsemani ndi ndani Yesu atatha kupemphera?**

Yudasi, ndi asilikali ambiri kudzagwira Yesu. (Mateyu 26:45-50)

**VESI LOLOWEZA:**

"Ichi ndi mwazi wanga wa chipangano ,wothiridwa chifukwa cha anthu ambiri". (Mariko 14:24)

**PHUNZIRO 18**  
**IMFA YA YESU PA MTANDA**  
**Mateyu 27 ndi Luka 23**

**1. Kodi Yesu anafa bwanji?**

Anakhomedwa pa mtanda pakati pa zigawenga ziwiri. (Mateyu 27:38)

**2. Kodi mawu oyamba amene Yesu ananena pa mtanda paja anali otani?**

"Atate, akhululukireni iwo chifukwa sadziwa chomwe akunena". (Luka 23:34a)

**3. Kodi m'modzi mwa zigawenga zija anapempha chiani Yesu?**

"Ambuye, ndikumbukireni ine mukamalowa mu ufumu wa kumwamba. (Luka 23:42)

**4. Kodi Yesu anayankha chiani chigawenga chija?**

"Lero lomwe, ndidzakhala nawe ku mparadiso. (Luka 23:43b)

**5. Chinachitika ndi chiani masana?**

Mdima unadzadza dziko lonse ndi mantha akulu anagwera anthu onse okhalamo. (Mateyu 27:45, 54; Luka 23:44)

**6. Ndi chifukwa chiani Yesu analira kumapeto kwa m'dima?**

'Mulungu wanga" Mulungu wanga mwandisiyiranji Ine? (Mateyu 27: 46b).

**7. Chinachitika ndi chiani Yesu atafa?**

Chinsalu cha nkachisi chinang'ambika pakati ndipo kunali chivomerezi ndipo manda anatseguka. (Mateyu 27:51-52)

**8. Kodi anakaika mtembo wa Yesu m'manda ndi yani?**

Yosefe waku Arimateya ndi Nikodemo omwe anatenga mtembo wa Yesu pa mtanda ndikuika m'manda atsopano. (Luka 23:50-53; Yohane 19:38-42)

**9. Ndi chifukwa chiani Yesu anayenera kufa imfa ya pa mtanda?**

Chifukwa imfa ya pa mtanda ndi imodzi mwa imfa ya otembereredwa. (Agalatiya 3:13)

**10. Ndi chifukwa chiani Yesu anafa imfa yotembereredwa?**

Amene anasenza machimo athu mwini yekha m'thupi mwache pa mtanda. (Agalatiya 3:13; 1 Petulo 2:24 ndi 1 Atesalonika 5:9-10)

**VESI LOLOWEZA:**

"Zoonadi Iye ananyamula zowawa zathu, ndi kusenza zisoni zathu "(Yesaya 53:4a)

**PHUNZIRO 19**  
**YESU AUKA KWA AKUFA**  
**Mateyu 27-28,Luka 24 ndi Yohane 20**

**1. Kodi Yesu anaikidwa kuti?**

Anayikidwa m'manda a tsopano a Yosefe wa ku Arimateya. (Mateyu 27: 57-60)

**2. Kodi Ayuda anateteza bwanji Yesu m'manda?**

Anauza Pilato kuti ayika asilikali kumanda. (Mateyu 27:62-66)

**3. Chinachitika ndi chiani mbanda kucha wa tsiku lakuyamba la sabata?**

Yesu anauka kwa akufa. (Mateyu 28:1-6; Luka 24: 1-6, Yohane 20:1, 11-16)

**4. Kodi Ambuye anadziwonetsa bwanji kuti wauka?**

Mngelo wochokera kumwamba anakunkhuniza mwala pa manda. (Mateyu 28:2)

**5. Kodi mngelo anawauza chiani amayi omwe amapita kumanda kunja?**

"Sali muno, pakuti wauka monga ananenera, onani mmunda momwe anagona Ambuye mulibe" (Mateyu 28:6)

**6. Kodi amayi aja anawona chiani mmene anayang'ana mmanda momwe Ambuye anagona?**

Anaona nsaru zabafuta zakumanda zitakhala, koma Yesu anali atauka. (Yohane 20:4-7)

**7. Kodi anali woyamba kumuona mpulumutsi ndi yani?**

Mari Magalena, yemwe amalira kumanda kunja. (Yohane 20:11-16)

**8. Kodi Ambuye Yesu anaonekera kwa ophunzira ake tsiku lomwero?**

Inde, Iye anaonekera madzulo pamene zitseko za zipinda zinali zotseka. (Yohane 20:19)

**9. Kodi kunali kofunika bwanji kuti Yesu apachikidwe tsiku loyamba la sabata?**

Ambuye Yesu anasinthia sabata yathu kuchokera tsiku la chisanu ndi chimodzi kufika tsiku la chisanu ndi chiwiri ndicholinga choti tisangalale ndikuukitsidwa kwache. (Chibvu 1:10; Machitidwe 20:7; 1 Akorinto 16:1-2)

**10. Kodi kuuka kwa Yesu mmanda kumatilimbikitsa chiani anthufe?**

Kuti Ambuye Yesu adzatiukitsa ife kuuzimu ndi kuthupi. (1 Akorinto 15:20-22; Afilipi 3:8-11; 1 Petulo 1:3-5; 3:21-22)

**VESI LOLOWEZA**

"Koma tsopano Kristu waukitsidwa kwa akufa chipatso choundukula cha iwo akugona" (1 Akorinto 15:20)

**PHUNZIRO 20**  
**ADZAZIDWA NDI MZIMU WOYERA**  
**Machitidwe 1 -2**

**1. Kodi Ambuye Yesu anakwera liti kumwamba?**

Anakwera kumwamba patatha masiku makumi anayi (40) atauka kwa akufa.  
(Machitidwe 1:2-3; 9-11)

**2. Kodi Yesu anawauza ophunzira kuti achite chiani asanawachokere?**

Anawauza kuti adikilire mzimu woyeru mu Yerusalem. (Machitidwe 1:4-5)

**3. Kodi Ambuye Yesu pano akuchita chiani kumwamba?**

Akulamulira pa zinthu zonse za kumwamba ndi za pansi pano. (Aefeso 1:20-23; Ahebri 1:1-2)

**4. Kodi chinanso chomwe Ambuye Yesu akuchita kumwamba ndi chiani?**

Akutipempherera ife tonse kwa Atate. (Aroma 8:34; Ahebri 9:12, 24)

**5. Kodi Atate amayankha bwanji pemphero la Ambuyeli?**

Atate amaperekwa kwa Yesu madalitso onse omwe ife timawafuna. (Aefeso 4:7-8)

**6. Kodi dalitso loyamba lomwe Yesu anaperekwa kwa ife linali lotani?**

Mzimu woyeru unatsanulidwa pa tsiku la pentekoste. (Machitidwe 2:1, 4)

**7. Kodi chizindikiro chomwe chinaperekedwa kuti mzimu unatsanulidwa chinali chotani?**

Panamveka chipokoso ngati nkokino wa mphepo yayikulu. (Machitidwe 2:2)

**8. Ndi chizindikilo chanji china chomwe chinaperekedwa?**

Malilime ngati a moto kwa anthu zana limodzi ndi makumi awiri (120) omwe anasonkhana pa chipinda cha pamwamba. (Machitidwe 2:3)

**9. Kodi anthu zana limodzi ndi makumi awiri (120) aja anapatsidwa mphamvu zapadera zotani?**

Anayamba kulankhula nzilankhulo zosiyanasiyana. (Machitidwe 2:4-12)

**10. Kodi kuyankhula ndi ziyankhulo zosiyanasiyana chinali chizindikilo chotani?**

Chinali chizindikilo choti Mulungu tsopano asonhanitsa anthu ake kuchokera m'maiko onse a dziko lapansi. (Machitidwe 2:14-21, 39)

**VESI LOLOWEZA:**

"Yesu amene waladiridwa kunka kumwamba kuchokera kwa inu, adzadza momwemo monga munamuona alinkupita kumwamba". (Machitidwe 1:11b)

**PHUNZIRO 21**  
**PETRO ACHIRITSA MUNTHU WOPUWALA**  
**Machitidwe 3-4**

**1. Kodi Petro ndi Yohane anachita chiani patangotha Pentekoste?**

Anapita ku kachisi kukapemphera. (Machitidwe 3:1)

**2. Kodi Petro ndi Yohane anaona ndani pa chipata cha kachisi?**

Anaona opempha yemwe anali olumala kwa zaka makumi anayi. (Machitidwe 3:2-5; 4:22)

**3. Kodi Petro ananena chiani kwa munthuyu?**

Anamuza kuti ayime ndikuyenda. (Machitidwe 3:6-7)

**4. Kodi Petulo anachita izi mu dzina la ndani ?**

Mudzina la Yesu, owukitsidwa. (Machitidwe 3:6)

**5. Kodi munthu olumala uja anakhulupirira zoti Yesu angamumuchiritse?**

Inde, mulungu anamupatsa iye chikhulupiriro kuti akhulupirire Yesu. (Machitidwe 3:8-9)

**6. Kodi munthu olumala uja anachira?**

Inde, anadumphadumpa ndikuyamika Mulungu. (Machitidwe 3:8)

**7. Kodi zotsatira za chozizwa chimenechi zinali zotani?**

Anthu ambiri anabwera ndikumvera Petulo akulalikira za Ambuye owukitsidwayo. (Machitidwe 3:11-12)

**8. Kodi izi zinakwiyitsa akuluakulu?**

Inde, anakwiya kwambiri ndipo anaika Petulo ndi Yohane m'ndende. (Machitidwe 4:1-3)

**9. Kodi akuluakulu anawauza chiani Petro ndi Yohane tsiku lotsatira?**

Anawauza kuti asayankhulenso m'dzina la Yesu. (Machitidwe 4:5-6, 18)

**10. Kodi Petro anawayankha chiani?**

"Sitidzachita koma kuyankhula zinthu zimene tinaziona ndi kumva. (Machitidwe 4:20)

**VESI LOLOWEZA:**

"Weruzani ngati nkwabwino pamaso pa Mulungu kumvera inu koposa Mulungu"(Machitidwe 4:19)

**PHUNZIRO 22**  
**PETRO ALALIKIRA KWA KONOLIYASI**  
**Machitidwe 9-10**

**1. Ndi chifukwa chiani Petro anapita ku Samariya?**

Petro anapita ku Samariya kuti akalalikire kwa okhulupirira. (Machitidwe 9:32)

**2. Kodi Ambuye Yesu anaonetsa bwanji mphamvu kupiyolera mwa Petro?**

Petro anachiza Enaya yemwe anadwala zaka zisanu ndi zitatu. (Machitidwe 9:33-34)

**3. Kodi ndi chozizwa chanji chimene Petro anachita ku Yopa?**

Petulo anaukitsa Dorika ku imfa. (Machitidwe 9:37-41)

**4. Kodi Petro anaona masomphenya anji ku Yopa?**

Anaona masomphenya a zinyama ndi mbalame zomwe Ayuda samaloledwa kudya. (Machitidwe 10:9-13)

**5. Kodi Petro anayankha chiani pamene Ambuye anamuza kuti atenge ndi kudya?**

Anayankha kuti iye sanadyepo ndi kale lomwe kanthu wamba ndi konyasa. (Machitidwe 10:14)

**6. Kodi Ambuye anamuza chiani Petro?**

Anamuza kuti "Chomwe Mulungu anayeretsa usachiye chinthu wamba. (Machitidwe 10:15)

**7. Ndi chifukwa chiani Mulungu anaonetsa Petro masomphenya amenewa?**

Mulungu amafuna Petro kuti akalalikire kwa amitundu. (Machitidwe 10:34-35; 15:7-9)

**8. Kodi Petro anadziwa bwanji kuti tanthauzo lake linali lotere?**

Amuna anabwera kuchokera kwa Koneliyasi yemwe anali wa a mitundu ,anamufunsa Petro kuti apite ndikukalikira mawu kwa iye. (Machitidwe 10:19-22)

**9. Kodi Petro anapita?**

Inde, anapita ndikukalalikira za Ambuye Yesu ku banja la Konoliyasi ndi kwa abwenzi ake. (Machitidwe 10:23-36)

**10. Chinachitika ndi chiani pamene Petro anali kulalikira?**

Mzimu woyeru unatsika kwa amitundu ndipo anayankhula ndi malilime ena nalemekenza Mulungu. (Machitidwe 10:44-46a)

**VESI LOLOWEZA:**

"Malekezero onse a dziko lapansi adzakumbukira nadzatembenukira kwa Yehova"(Masalimo 22:27a)

**PHUNZIRO 23**  
**ULENDO WOYAMBA WA UTUMIKI WA PAULO**  
**Machitidwe 9 ndi 13-14**

**1. Kodi anali mboni ya Stephano pamene anali kugendedwa ndi miyala ndi ndani?**  
Analı Saulo wa Tarisi yemwe anavomereza za imfa ya Stephano. (Machitidwe 7:57 - 8:1)

**2. Ndi chifukwa chiani Saulo anapita ku Damasiko?**  
Amapita ku Damasko kuti akagwire Akhristu ngati akapolo akhristu ndi kuwatengera ku Yerusalem. (Machitidwe 9:1-2)

**3. Ndi ndani anaonekera kwa Saulo pa njira?**  
Ambuye Yesu anaonekera kwa iye nanena, "Saulo, Saulo undilondalonderanji ine?" (Machitidwe 9:4)

**4. Kodi Ambuye Yesu anamuitana Saulo kuti apange chiani?**  
Anamuitana Saulo kuti akalalikire uthenga wabwino kwa a mitundu. (Machitidwe 9:15)

**5. Kodi Saulo anapita ndi ndani pa ulendo woyamba wa utumiki wake?**  
Anapita nao Banarba ndi Yohane. (Machitidwe 13:1-5)

**6. Kodi dzina la Saulo linasinthika kukhala ndani?**  
Linasinthika kukhala Paulo. (Machitidwe 13:9)

**7. Chinachitika ndi chiani pa chisumbu cha Cyprus?**  
Oyang'anira chisumbu ndi anthu ena anapulumutsidwa. (Machitidwe 13:4-12)

**8. Kodi chotsatira cha uthenga umene Paulo analalikira ku Antiyokeya chinali chotani?**  
Amitundu ambiri anakhulupirira Yesu khristu. (Machitidwe 13:48)

**9. Kodi Ayuda anawonetsa bwanji nsanje kwa Paulo ku Antiokea mu Pisidiya?**  
Anathamangitsira Paulo ndi Barnaba kunja kwa mzinda. (Machitidwe 13:50)

**10. Kodi anthu osamvera a ku Lustra anachita chiani ndi Paulo ndi Barnaba?**  
Poyamba anafuna kuwapembeza ngati milungu koma potsiriza pake anamuponya paulo miyala ndipo anamusiya okufa. (Machitidwe 14:11-15, 19)

**VESI LOLOWEZA:**

"Mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa Olengedwa onse" (Mariko 16:15)

**PHUNZIRO 24**  
**ULENDO WACHIWIRI WA UTUMIKI WA PAULO: MACHITIDWE 16-18**  
**Machitidwe 16**

**1. Kodi Paulo ndi Sila anapita kuti pa ulendo wao wa chiwiri?**

Anapita ku Suriya kukayendera ndi kukhazikitsa mipingo. (Machitidwe 15:40 - 16:2, 6)

**2. Ndi masomphenya otani omwe anafikira Paulo ku Trowa?**

Paulo anaona munthu wa Makedoniya yemwe anati, "Muolokere ku Makedoniya kuno mudzatithangate ife" (Machitidwe 16:9)

**3. Kodi masomphenya amenewa amatanthauza chiani?**

Amatanthauza kuti Mulungu anaitanira iwo kulalikira mu Makedoniya. (Machitidwe 16:10,12)

**4. Kodi woyambirira kupulumutsidwa ku Makedoniya anali ndani?**

Lydia yemwe anabatizidwa ndi a pa banja lake. (Machitidwe 16:14-15)

**5. Kodi mtsikana wa mzimu wonyasa analilira kwa Paulo ndi Sila kuti chiani?**

"Anthu awa ndi akapolo a Mulungu wa kumwambawamba amene akulalikirani inu njira ya chipulumutso" (Machitidwe 16:17)

**6. Kodi chinachitika ndi chiani pamene Paulo anachotsa mzimu wonyasa uja?**

Paulo ndi Sila anamenyedwa ndikuponyedwa m'ndende. (Machitidwe 16:19-24)

**7. Kodi Paulo ndi Sila amaopa m'ndende muja?**

Ayi, pakati pa usiku anali kuimba nyimbo zolemekeza Ambuye. ( Machitidwe 16:25)

**8. Kodi Mulungu anaonetsa bwanji mphamvu yake?**

Kunagwa chivomerezi chachikulu chotero kuti maziko andende anagwedezeza pamenepo makomo anatseguka ndimaunyolo a Paulo ndi Sila anamasuka. (Machitidwe 16:26)

**9. Kodi oyang'anira ndende anachita chiani?**

Anadandaulira Paulo ndi Sila nati, "Ambuye ndichitenji kuti ndipulumuke"? (Machitidwe 16:30)

**10. Kodi Paulo ndi Sila anawayankha chiani a dindo a ndende?**

Khulupirirani pa Ambuye Yesu khristu ndipo mudzapulumuka inu ndi a panyumba yanu. (Machitidwe 16:31)

**VESI LOLOWEZA:**

"Pakuti lonjezano liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa ana anu ,ndi kwa onse akutali onse amene Ambuye Mulungu wathu adzaitana" (Machitidwe 2:39)

**PHUNZIRO 25**  
**ULENDO WACHITATU WA UTUMIKI WA PAULO**  
**Machitidwe 19-28**

**1. Kodi Paulo anapita kuti paulendo wake wachitatu?**

Anapita ku Aefeso komwe anagwira ntchito kwa zaka ziwiri. (Machitidwe 19:1a,10)

**2. Kodi anthu ambiri anaonetsa bwanji chikhulupiriro chao mwa Mulungu?**

Anasonkhanitsa mabuku ao nawatentha ndi moto. (Machitidwe 19:18-19)

**3. Kodi anatsutsana ndi Paulo ku Aefeso ndi ndani?**

Demetriyo yemwe amasula tiakachisi ta siliva ta ka mulungu kotchedwa Diana. (Machitidwe 19 :23-25)

**4. Ndi chifukwa chiani Demetriyo anatsutsana ndi Paulo?**

Amaopa kuti Uthenga wa Paulo ukandalowetsa pansi ntchito yake. (Machitidwe 19: 25-27)

**5. Kodi chinachitika ndi chiani pamene Demetriyo anapanga upo ndi anthu motsutsana ndi Paulo?**

Mu m'zinda monse munachita piringu-piringu ndipo Paulo anathawa ku Aefeso. (Machitidwe 19:28-30; 20:1)

**6. Kodi Paulo anapita kuti atachoka ku Aefeso?**

Anapita ku Makedoniya ndi ku Greece. (Machitidwe 20:1-2)

**7. Kodi mzimu woyer aamuza chiani Paulo pa ulendo wake?**

Anamuza kuti iye akatsekeredwa m'ndende ku Yerusalem. (Machitidwe 20:22-23)

**8. Ndi chifukwa chiani Paulo anatsekeredwa m'ndende?**

AYuda osakhulupirira onse anamunamizira iye kuti ali kuphwanya malamulo a Mose. (Machitidwe 21:20-21, 28-37)

**9. Kodi Ambuye anamulondolera kuti Paulo ngati wa M'ndende?**

Anamulondolera ku Roma kuti akalalikire Uthenga kumeneko. (Machitidwe 23:10-11; 28:14-16, 23-24, 30-31)

**10. Kodi chotsatira cha Uthenga umene Paulo amalalikira chinali chotani?**

Uthenga unafalikira m'maiko ambiri ndipo anthu anakhulupirira mwa Ambuye Yesu Khristu. (Machitidwe 28:28; Afilipo 1:6-20; 2 Timoteyo 2:9-10; Filimoni 10 mpaka kutsokoloko)

**VESI LOLOWEZA:**

"Ndalimbana nako kulimbana kwabwino ndatsiriza njirayo ndasunga chikhulupiriro"(2 Timoteyo 4:7)